LESSON 21 HERE and THERE

| | | | |
|---|---|---|---|
| **Gule 1** | dance 5 | **-vina** | dance |
| **Ng'oma** | drum | **-onera** | look at, attend |
| **Mbendera** | flag | **-pachika** | suspend, hang |
| **Mpira** | ball | **-lamula** | order, command |
| **Mtundu** | kind, tribe | **-kana** | refuse, deny |
| **Nyimbo** | song, hymn | **-nama** | lie |
| **Chithunzi** | picture | **-onetsa** | show |
| **Sewero** | play, game | **-imba** | sing |

Here we find the list of Locatives corresponding to the four Demonstratives **uyu, uyo, uno, uja.** To understand the precise meaning of each word, we must remember the difference between the three Prepositions **Pa, Ku, Mu;** and also between the four Demonstratives **uno, uyu, uyo, uja.**

| | WHERE | | HERE | | THERE | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| **PA** | on................ | **Pati?** | **Pano** | ......**APa** | **Apo** | ......**Paja** |
| **KU** | at, in, to ...... | **Kuti?** | **Kuno** | ......**Uku** | **Uko** | ......**Kuja** |
| **MU** | in, inside ...... | **Muti?** | **Muno** | ......**Umu** | **Umu** | ......**Muja** |

**Pati?** on which spot? **Ndiike pati nsungwizi? Ndikhale pati?**
**Pano** on this spot where I am. **Pamudzi pano ndi pa yani?**
**Apa** on this spot close to me. **Khalani pampandopa!**
**Apo** on that spot over there. **Khola lao la ng'ombe lili apo....**
**Paja** on "the" spot, you know which. **Wasiya chipewa pampando paja.**

**Kuti?** in which area, direction? **Anthuŵa amakhala kuti?**
**Kuno** in this area where we are. **Bwerani kuno! Kuno kuli njala.**
**Uku** in this area near. **Kakhaleni kubwalo uku!**
**Uko** in that area over there. **Kwa Chimutu ndi uko.**
**Kuja** in the area, you know which. **Mfumu akapitanso kumudzi kuja.**

**Muti?** in which room. **Ana anu amagona muti, umu kapena umo?**
**Muno** in this room where I am. **Pirikitsa garu, asalowe muno!**
**Umu** in this room, near. **Chenjerani; mnyumba umu muli zoluma.**
**Umo** in that room over there. **M'nyumba umo simugona anthu.**
**Muja** in "the" room, you know which. **Malaya ako ali m'nyumba muja.**

**-ponya mpira: -menya mpira: -sewera ndi mpira** play football
**-imba ng'oma: -omba ng'oma: -liza ng'oma** beat the drum
**-soka mphasa: -luka mkeka: -luka dengu**
**-imba**...play an instrument : **-bisa mawu** hide the truth
**-kana** refuse: **Ndinamuuza kuti asese umu; koma iye anakana.**
deny: **Ndinamfunsa kuti: Kodi ndiwe unaba malaya? Koma anakana.**
(wa) **mitundumitundu** of many kinds: **Ndinagula zinthu za mitundumitundu.**
**-jambula chithunzi** take a picture: **-jambula** draw

Suffixes **-po -ko -mo** : In the translation of "there is", we have met these suffixes corresponding to the Prepositions **Pa, Ku, Mu: -lipo -liko -limo.** They can be added to other verbs as well:

**Mnzanga adapita kunyanja dzana. Inenso ndipitako mawa.**
**Chotsani katundu patebulo apa kuti ndiikepo mbalezi!**
**Ndinamva kuti munali kumaliro. Mwabwerako nthaŵi yanji?**
**Kodi kumudzi kwathu munafikako? — Iyayi, kwanu sindidziŵako.**
**Lamulungu anafika kutchalitchi; koma sanaloŵemo.**
**Mundipatse nyale ija kuti nditsiremo mafuta.**

**Dziko la pansi pano** earth: world **Dziko la Kumwamba** heaven

1. The Malaŵi flag is black, red and green. It is on the top there.
2. Go and play together with your companions on the football ground!
3. On the wedding feast there will be dances of all kinds.
4. The school children gathered in front of the church and sang hymns.
5. Do you know the girl who is on that picture? What is her name?
6. I told him to clean the ground, but he refused.
7. What song shall I sing? — That one which you sang last week.
8. The girls of Chimutu village came to dance here two weeks ago.
9. Where have you put the picture which I left here yesterday?
10. You say that you did not steal the shoes. You are a liar.
11. My younger brother went to the lake last year and stayed there 2 months.
12. I will come again to-morrow to show you the pictures.
13. Tie the string to the tree so that I may hang the clothes on.
14. If you have a basket, bring it, and I will pour in some maize.
15. If you have a headache, don't stay in the sun, come and sit here.

**Proverb: Wopusa anaomba ng'oma, ochenjera nabvina.**